**PROVISIONAL MARKING KEY**

**CHICHEWA III**

## GAWO A

**1.** a. Munthu amene akupepesa mayi ake chifukwa cha khalidwe lake loipa.

b. i. Amasowa zovala zabwino.

ii. Amasowa chofunda

/Amasoweka mchere

c. i. N’chiguduli/N’dzanjalidi/n’kutukumuka/ngochita

ii. Nsanza ndi nsabwe /N’chiguduli ndi n’dzanjali

iii. Kwanga n’kutukumuka ngati finye

d. i. Kuthyola

ii. Thoo

iii. Phala

e. i. Mwamwano

ii. Uchidakwa

/Ulesi/Kusayamika/Kasakhazikika pakhomo

f. Kupepesa/Kuthokoza/Kugonja

g. Ndevu adafika potopa nazo kumeta.

## GAWO B

2a. Ya mkambazawina

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

b. i. Chining'a

-zidawamwa njuchi/ anthanga imodzi/ adatchuka/ kachikho/ adapezeka/ adawamata phula/

muzu waulesi

ii. Ntchedzero

-Moyeyeka ngati kamwana ka nkhunda

iii. Chifaniziro

-Zidawamwa njuchi/ Adawamata phula

c. i. Yomwera mankhwala

ii. Sabereka

iii. Kachibwenzi

iv. Kunamizana

**d.** -Makolo a Gobani adakwiya ndi kusalemba ntchito kwa mwana wawo yomwe a phunzitsi amapereka.

-Amaganizira kuti mwana wawo amalowa m'kalasi pomwe mwana wawo samalowa.

**e.** lachikondi

loyanjanitsa

**f.** Makolo ake amafuna kumukonza khalidwe Gobani atawonongeka kale zomwe sizidasinthe kanthu.

3a. Makhalidwe oipa a Nthondo.

- Kuba
- Nkhanza
- Kuuma mtima
- Ulesi
- Mwano

b. Chikondi cha atengambali ena.

- Ena adathandiza kutenga madzi pa chikuta cha Nthondo
- Ena adathandiza kumanga denga la nyumba ya amake Nthondo
- Anzake a Nthondo adamuthandiza kufuna ntchito ku Harare

Downloaded for **FREE** from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

- Ena adayenda naye Nthondo kuchoka ku Harare anzake atamuthawa
- Azungu adapereka mabulangete kwa anthu am'mudzi
- Atadwala Nthondo azungu adamupititsa ku Chipatala.
- Anthu adathandiza pa maliro a bambo komanso atsibweni a Nthondo.

**4.** a. i**.** AMgezenge

**-**Amamumenya Nagama

**-**Adachititsa ukwati ndi kamwana kakang'ono dzina lake Zikani.

**-**Adalemba ntchito mwana wamng'ono dzina lake Funsani.

**-**Amafuna Funsani azigulitsa mugolosale yawo akudwala.

**-**Amafuna mkazi wawo azigwira ntchito akudwala.

ii**.** Gama

**-**Adalephera kumulipilira Zikani ndalama yakusukulu.

**-**Adamukwatiwitsa Zikani akadali wamng'ono.

**-**Adamusiyitsa sukulu Zikani.

**-**Amafuna Nagama azikhala kubanja komweko ngakhale amamenyedwa ndi a Mgezenge.

iii**.** AMackson chikoya

**-**Adamukhalitsa Mayamiko ku sukulu kuti akagulitse nkhuni.

**-**Adamusenzetsa chimtolo chachikulu chankhuni chosafanana ndi msinkhu wa Mayamiko.

iv**.** Bambo ake a funsani

**-**Adamusiyitsa sukulu.

**-**Adamulowetsa ntchito akadali wamng'ono.

v**.** Bambo a Chisomo mwakiyale

**-**Adavomereza kuti Chisomo akwatiwe ndi a Mwenechanya ngati njira yobwezera ngongole.

zomwe anali nazo.

-Adamusiyitsa sukulu.

vi**.** kamwendo

**-**Ana awo amawakhalitsa ku sukulu kuti akagwire ntchito ya kumunda ndi pakhomo.

**-**Amawagwiritsa ntchito ana awo zodutsa msinkhu wawo.

**-**Amatenga malipiro antchito yomwe agwira ana awo.

**b. i.** kuwonongeka kwa chilengedwe

-M'mudzimo mulibe chimanga.

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

-Mnyanja mulibe nsomba monga nthachi , nkhututu, mbununu, chitemera ndi nkhalala.

-Mu nkhalango mulibe zipatso zam'tchere monga masuku, nziru, kankhande, maye, nthudza, bwemba, mapoza ndi kasokolowe.

-Mulibe mitengo ya mankhwala monga mvunguti, msolo, kamphuri, msambamfumu, mwavi ndi thundu.

-Mitengo ina yomwe mulibe ndi monga mgwalangwa,msopa, mkongomwa ndi mKalati

-kutha kwa nyama monga akalulu, agwape, mbawala ndi ntchenzi.

-Nyengo yasintha mvula ikugwa mwanjomba.

-Ngozi za chilengedwe zikuchitika pafupipafupi.

**ii.** Nkhanza kwa amayi.

-Amayi akumenyedwa ndi amuna awo chifukwa choti abwera mochedwa kokatola nkhuni.

-Azibambo akukadya ndalama zomwe apeza pa ulimi ndi akazi ena.

**iii.** Nkhanza kwa ana.

-kugwiririra ana ang'ono.

-Aphunzitsi kufunsira atsikana.

**iv.** zoipa zomwe achinyamata akuchita.

-Alowelera akumwa mowa komanso kugwiritsa ntchito mankhwala ozunguza bongo

-Sakuvala moyenera akuyenda bele lili pamtunda, akuvala ndekesha.

-kusokoneza pa misonkhano yandale.

-Akuyambitsa zipolowe.

-Anthu ena anavulala.

-Ena anaphedwa.

**v.** kusalana kaamba kamtundu ndi zipembedzo

-Akusalidwa pa ntchito monga zolima misewu zomwe amalandilapo ndalama.

-Akusalidwa pa zinthu zaulere monga chakudya zomwe mabungwe amapereka.

Downloaded for **FREE** from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

**MAYANKHO ATHERA PANO**

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com